

TSAMBA LA NKHANI

ENDTIME

M E S S E N G E R S



ZOCHITIKA
MAY 2025

Pope inauguration Mass
BBC NEWS 6:05

Pope Leo XVI's inauguration Mass takes place at Vatican | BBC News
BBC News · 3.7K views · 54 minutes ago

TAKULANDIRANI

M'MASIKU a M'DIMA

MASIKU A KUMAPETO

- ◇ **MULUNGU NDI NDANI?..... 1**
- ◇ **BANJA LA CHIKHRISTU..... 2**
- ◇ **MAUMBONI A KUTEMBENUKA
MTIMA KWA ANTHU..... 3**
- ◇ **ZOZIZWA ZA MAKONO ANO. 4**
- ◇ **MASOPHENYA NDI MALOTO. 5**
- ◇ **MZIMU WACHINENERO..... 6**
- ◇ **NDAKATULO CORNER 6**
- ◇ **TILIPATI MU ULOSI..... . 7**
- ◇ **ZAKUDYA ZOYENERA..... 8**
- ◇ **SABATA KAPENA SUNDAY?.. 9**
- ◇ **ADZIWENI ATUMIKI ANU..... 11**
- ◇ **INU NDI NTHANZI LANU 13**
- ◇ **DZIWANI NYIMBO ZA UZIMU. 15**



**palibe sing'anga
aliyense yemwe
wandichiritsa ko-
ma Mulungu .
TSAMBA 3**

**“Mkazi odziwa mavuto,
opilira komanso
n’thandizi mu utumiki”
kwinaku
akumwemwetera.
TSAMBA 11**



**....okana kuti Mulungu
kulibe akuchuruka tsiku
ndi tsiku TSAMBA 1**

**Akulu akale anati “Mwana
akalilira nyanga ya msatsi,
msemere imfotere yekha.
Ndiye ine kapena inu mukad-
wala sivuto la Mulungu koma
vuto lathu. Mulungu sanapan-
ge munthu kuti adzadwala
TSAMBA 13**





MULUNGU NDI NDANI?

WOLEMBA :

EV.YANKHO MALIZANI

Genesis 1:1— PACIYAMBI Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.

Mu cholembedwa ichi tikhala tikufukula Kuchokera m' buku lopatulika Bible, zikhaliidwe za anthu, mu chilengedwe pa chokha ndi zolemba zina pofuna kuyankha funso loti **KODI MULUNGU NDI NDANI?** Mulungu ndi Ndani? Kodi Mulungu alipo? Nanga Kodi Mulunguyo Anachokera kuti?

Awa ndi ena mwa mafunso omwe anthu ambiri polephera kupezera mayankho olondola adagwa mphwayi ndikuyamba kunena kuti Mulungu kulibe.

Mlembi wa tsambali akulemba ndi malingaliro otseguka, osatsamira pa chipembedzo chilichonse koma Ku choonadi ndi chilungamo chokha pa chidziwitso chotsamira kwamabiri Ku mau a Mulungu Mwini. Tikukhala mu nthawi imene anthu ambiri okana kuti Mulungu kulibe akuchuruka tsiku ndi tsiku, komanso ambiri akuchita chiganizo chosiya kupita Ku Malo opembedzera mmakachisi, Iwo akuchita ziganizo zoterezi pa zifukwa zosiyanasiyana

Kungochulapo zifukwa zowerengeka

⇒ **Mavuto a Moyo Uno, umphawi, matenda, Kutha Kwa mabanja kamba Ka mavutowa Iwo akuona kuti owasamala palibe**

⇒ **Ena kugwetsedwa mphwayi ndi atsogoleri azipembedzo, akhanza komanso osakhulupirika**

⇒ **Kusatembenuka mtima, ambiri amawuyamba ulendo otsatira Mulungu koma malingaliro awo asanawapereke mmanja a Mulungu**

Izi ndi zina mwa zifukwa zochepe chabe zomwe zikuchititsa anthu kuti ataye chidziwitso chawo pa Mulungu. Nalo Buku lomalizira mu Bible likutsimilizira ganizo ili kuti alipo olenga ndi kupanga zinthu zonse, iye ndiye Mulungu

Cibvumbulutso 14:7

Ndi kunena ndi mau akuru, OPANI

MULUNGU, MPATSENI

ULEMERERO; PAKUTI YAFIKA

NTHAWI YA CIWERUZIRO CACE;

Kodi Mulungu uyu ndi Ndani?

Tsamba lino liyesetsa kufukula ndi kukupatsani kuya Kwa mayankhidwe a funso limeneli ndi kuthangatira maganizidwe Anu pa za Mulungu monga Mlengi

Mulungu ndi Mlengi.

Bible (Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu mu Genesis 1:1 latitsimikizira kuti Pachiyambi Mulungu adalenga Kumwamba ndi dziko lapansi. Kusonyeza kuti zinthu zonse za m'wamba, zapadziko ndi pansu pa dziko alipo wina adazipanga, ameneyo ndiye Mulunguyo. Mwachitsanzo Chiuta ndi dzina logwiritsidwa ntchito pakati pa Atumbuka omwe ali kumpoto Kwa Malawi komanso Zambia..

Dzina loti Chiuta Pena amati Mulengi, olenga zonse, Namalenga. Ndi dzina lomwe

limanthauza kuti wamkulu, wapamwamba, Wamphamvu oposa chinachilichonse. Zilankhulo zina Ku Malawi kuno amati Chiuta, Namalenga, Mphambe, ndi maina ena ndi ena owonjezera koma onsewa amalumikizana ndi dzina loti Mulungu.

Ndipo izi zili chimodzimodzi ndi zilankhulo zonse za chibanthu (mitundu yamu Africa) pa-fupifupi zilankhulo 30 zimagwirizana pa dzina ili. Ku chiswahili dzina loti Mulungu limalembedwa kuti Mungu, koma poyambilira maphunziro achiluya MU chipembedzo cha chisilamu pofika pakati pa a Swahili adali kugwiritsa ntchito dzina loti Mulungu, koma pakadali pano dzina loti Mungu ndilomwe limamveka kwambiri. M' fundo izi zonse zikutipatsa chitsimikizo choti ngakhale azungu ndi aluya asanabwere ndi chikhristu komanso chisilamu pakati pa a banthu, makolo anthu kalelo amadziwa ndithu kuti alipo wina Wamphamvu ndi wapamwamba oposa zonse koma iwo adali kukhala opanda chidziwitso chakuya pa za Wamphamvu zonse ameneyu. **PANGANI CHISANKHO CHOMUDZIWA MULUNGU MLENGI WANU. DZIWANU ZAMMAWA SIZIDZIWIKA... MOYO NDI LERO**

Yesetsani kupeza Bible mudziwerenga, ngati mulinalo kale koma simumawerenga yambani po kukhulupilira ndi kuwerenga ndipo mudzakuzubale wanu ndi Mulungu. Chisankho ndi lero pakuti za mmawa sizidziwika. Mulungu alipo ndipo ndi Mlengi wanu.

Miyambo 4:7 — Nzeru ipambana, tatenga nzeru M'kutenga kwako konseko utenge luntha.





MALANGIZO KWA MABANJA ANG'ONO ANG'ONO



Wolemba

Esther Scott

Zokambirana zathu zikutsogoza ndi mau amene akuchokera pa

Miyambo 18 vs 22

pali mau akuti

wapeza mkazi apeza chinthu chabwino Yehova amkomera mtima.

kutanthauza kuti Banja ndi chinthu cha ulemu kwambiri komanso chinthu chodalitsika

Ana anga anyamata ndi atsikana masiku ano tamvetserani malangizo a ine mayi wanu

Ndikufuna ndipereke malangizo makamaka kwa mabanja ang'onoang'ono amene ndapeza kuli ali pa chiopsyeyo chachikulu kuti sakuchedwa kutha (sakulimba).

Ndimadzifunsa funso kuti kodi ndi chifukwa chiyani chikupangika kuti mabanja adzisokonekera motere? Mau a Mulungu akutitsimikizira kuti Yesu akakhala m'banja, banjalo limakondwa, Vuto ndi lakuti mabanja ambiri masiku ano aman-gomenyana ndi kuyambana kukhalira limodzi osasata ndondomeko yoyenera chinthu choipa ichi.



Mabanja ambiri sakumakhala ndi chikondi cheni cheni koma akumatsata chuma chimene wina ali nacho ,kapena maphunziro amene wina ali nawo ,kapena maonekedwe okongola amene wina ali nawo izinso sizabwino.

Mau a Mulungu pa

Miyambo 31 vs 30

akuti kukongola kungoyenga maonekedwe okoma ndi chabe koa mkazi woopa Yehova adzatamandid-wa. Amen

Maphunziro asapangitse anthu kukhala okulirana mitima. Ulemu ndi ofunika kwambiri m'banja monga Bible limanena kuti mwamuna ndiye mutu wabanja apatsidwe ulemu wake woyera ,mwamuna akonde, mkazi amvere.

- ◆ Mabanja ena akumayika ntchito pa tsogolo kulolera kuti wina adzikhala ku Blantyre wina karonga choopsya kwambiri ichi.
- ◆ Mabanja ambiri akutha chifukwa kusakhulupirika. tiyeni tidziwe kuti thupi limodzi sili-gawanika pakati ai
- ◆ Dziwani Chimanga banja ndi chikondi choona osati chuma ai.
- ◆ Kaya pali ana kaya palibe ana khalani okhulupilika kwa wina ndi mzake.
- ◆ Ngati pali ana Makolo tengani mbali yayikulu yolera ana anu kuti akule mu chisomo cha Mulungu..
- ◆ Khutitsidwani ndi zinthu zimene Mulungu wakudalitsani nazo musasirire zinthu za anthu ena. 1 Timothy 6 vs 10 akuti muzu wa zoipa zonse ndiye chikondi chapa ndalama
- ◆ Ikani Mulungu pa tsogolo mu zonse khalani banja lokonda kupemphera mukatero Mzimu woyera adzukura banja lanu nthawi zonse namukhala okondwa. -

Ambuye akudalitseni nonse. –dziwani kuti Yesu Khristu Akubwera



ZOZIZWA M'MASIKU AMAKONO, TILI NAYE MULUNGU WAMOYO NDI WOSAMALA.

Tili ndi Chikhulupiliro kuti Mulungu yemwe anawachiritsa mayake a Mada ku nthenda yawo , ndi Mulungu yemweyonso yemwe adzamuchiritse Mada mu nthawi yake.

adalotanso maloto , Iwo adalota munthu wina akuwaitana kuti amudzutse mwana wawo uja kuti amuone , atamudzutsa

ndipomwe adaona mwana uja akuoneka modabwitsa ,

miyendo ndi mikono yake ikuoneka mosiyana ndi nthawi zonse komanso itasiya kugwira ntchito , apa Iwo pamodzi ndi amuna awo adakumbukira maloto aja omwe mayake a Mada adauzidwa kuti akapanda kulimba mkupemphera nthenda yawo ija



TAONANI MOMWE MAYAKE A MADA ADALANDILIRA MACHIRITSO AWO.

Tsiku lina mwezi wa number 8 atagona usiku mayiwa analota maloto, munthu wina akuwapemphelera ndipo atamaliza akuwapemphelera anawauza kuti " tadzuka" koma Iwo Poona kuti samayenda anadabwa nawo mawu amunthuyu, komabe anayesera kudzuka kuti anyamule ndodo yawo yomwe akhala akuyendera ija, koma munthu

uja anatenga ndodoyo ndikumaizembetsa kuti mayake a Mada asaigwire uku akuwauzabe mawu aja okuti "tadzuka" ndipo anapitilira kunena kuti "tayasera kugwira khoma kuti udzuke " ndipo Iwo anagwira khoma lija ndikudzuka nalo , koma kuti uime bwinobwino, kenako adawauza mayiwa kuti tasiya khomalo zinditsata momwe ndikuyendera ineyo , ndipo Iwo anayamba kumutsatira munthu uja pambuyo pake pogwiritsabe ntchito khoma lija mpaka panja.

KUPITILIZA.....

Uwu ndi umboni wa Mayi wina yemwe amakhala ku chikwawa ndipo mayiwa ali ndi



mwana wamwamuna waulumali dzina lake Mada wa zaka 15.

M'chaka Cha 2010, mayi wake a Mada anali woyembekezera ndipo atangobereka mwana munjira ya opaleshoni miyendo yawo inasiya kugwira ntchito , amakanika kuyenda mmalo mwake amkachita kukwawa pogwiritsa ntchito ndodo kwa Miyezi isanu ndi itatu (8) komano nthawi yonsezi anzawo anali akuyankhula kuti sadzayendanso ndipo amuna awo amawauza kuti ayende

mwa asing'anga kukafuna thandizo la vutoli, koma Iwo amakana ponena kuti adzayenda mu chifuniro Cha Mulungu .

MMENE MADA ADAYAMBIRA KUDWALA KWAKE

Izitu zidachitika mchaka chomwe chija cha 2010 chomwe Mada anabadwa , patatha mwezi umodzi atachira mayake a Mada



idzabwera kwa mwana wawo , ndipo awiriwa adakambirana zomutengera mwana uja kuchipatala,

Atafika ku chipatala kuja adamuyeza mwana uja ndikuwauza kuti mafuta amwanayo alekana . Adokotala adawauza kuti apite kunyumba koma adzabwerenso kudzakumana ndi dotolo woona zamafupa , Adokotala adawauza kuti apite kunyumba koma adzabwerenso kudzakumana ndi dotolo woona zamafupa , tsiku litafika adapitanso kuchipatala kuja komwe adakakumana ndi dotolo uja , yemwe adawauza kuti azingopanga naye masewera olimbitsa thupi mwana uja (physical exercise) Umu ndimomwe nthenda ya Mada idayambira .



WOLEMBA:

MARY WASI

**Chitani
mbali yanu
pothandiza
ena kuti
awone
chikondi cha
Mulungu**



**WOLEMBA:
MARY WASI**

palibe
sing'anga
aliyense
yemwe
wandichiritsa
koma
Mulungu

Akupitilira kumutsatira munthu uja , anaona kumalo kwina komwe kunali madzi ochuruka komanso oyera ndipo Iwo adamufunsa munthu uja kuti uku tikupitaku ndi kuti ? Ndipo munthu uja adati tiye udzingonditsata popeza komwe tikupitaku ndikomwe ukachiritsidwe , koma mayiwa adati sangakwanitse kukafikako koma munthu uja adawalimbisa nati tatsala

pang'ono ndipo ukafikako, ndipo adayendabe mpaka kufika kumadzi kuja, apa munthu uja adauza mayake a Mada kuti alowe mmadzi muja, koma Iwo adakana poopa kuti akalowa mmadzimo angathe kumira ,koma munthu uja adawauza kuti palibe chomwe chingachitike ndipo tichokanso kunoko bwinobwino.

Ndipo munthu uja adayamba kuwatsogolera mayiwa pang'ono ndi pang'ono kulowa mmadzi aja, ndipo



atafika pakati pamadzi munthuyo adawauza kuti ndikubwelera koma iweyo ukuyenera usambe madziwa Kasanu ndi Kawiri (7) ndipo munthu uja adatuluka mmadzimo nakaima kumtunda ndikuwauza mayiwa kuti samba ndili pompano , apa mayake a Mada anayamba kusamba munga umakhalira ubatizo uku munthu uja akuwawerenga Kasanu ndi Kawiri, atamaliza adawauza kuti basi tuluka wachiritsidwa , ndipo anatuluka ndikukamupeza munthu uja kumtunda komwe anaima, komwe adawauza mayiwa kuti kuyambira lero wachiritsidwa komano ukuyenera kulimba mtima popeza nthendayi ibwera kwa mwana wako ngati supemphera kwambiri .

YAKOBO 1: 27

Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi atate ndiwo: kucheza ndi ana amasiye ndi akazi amasiye m'chisautso chao, ndi kudziungira mwini wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi.

Apa onse adachoka kumadzi kuja ndikuwamba kuyendanso kubwelera kunyumba komwe adayambaso kuwapemphelera mayiwa , kenako munthu uja adatenga madzi omwe adali ozizira kwambiri ndikuwapta kuti amwe, atamwa madzi aja anawauzanso kuti wachiritsidwa ndipo kuyambira mawa uyambiranso kuyenda .

Chozizwitsa ndichakuti , mayiwa atadzidzimuka pomwe anagona anadzukadi mpaka kuka-pezeka pa balaza ndipo amunawo adawaitana kuti atenge ndodo yawo poopa kuti akhoza kugwa , koma Iwo adayendabe mpaka kufika panja , koma izi sizidalinsio maloto ayi koma zochitika zenizeni.

Amunawo aja ataona izi adawatsatira panjapo ndikuwafunsa modabwa kuti watuluka ndi chani , Iwo adati ndatuluka ndekha popandanso ndodo , ndipo adayamba kuwafotokozera amunawo maloto omwe adalota aja, ndipo kutacha mmawa adadzukadi ndikuyamba kuyenda zomwe zidapangitsa anthu onse ammudzi mwao kudabwa , apa Iwo adakwanitsa kupita okha kukasamba, kusambitsa mwana wawo uja komanso adakwanitsa kukasenza chidebe Cha madzi anthu akuona.

ndipo patapita sabata ndi masiku okwana awiri atachiritsidwa , mayake a Mada adalotanso maloto ena usiku atagona, apa Iwo adalotanso munthu uja atabwera kudawapopa miyendo yawo ndikuwauza kuti anaiwala kuwakonza miyendo yawo , ndipo atawakonza adati apa pokha wachiritsidwa, atadzidzimuka anapeza kuti miyendo ija ili bwinobwino kukwanitsanso ngakhale kuthamanga komanso kuiwongola bwinobwino ndi kuvala msapato , izi zinadabwitsa anthu ammudzi mwawo omwe anayamba kuwafunsa kwa sing'anga komwe adapita kuti ayambirensio kuyenda, koma mayake a Mada adati palibe sing'anga aliyense yemwe wandichiritsa koma Mulungu yekha , kuyambira pompo mpaka lero Iwo Ali bwino bwino tsopano.

KODI KUTI MADA ADZIYAMBA KUKONDA KUPITA KU TCHALITCHI CHIDACHITIKA NDI CHANI?

Nanga kuti banja la kwa Madalitso lidizidwidwe ndi ma messengers chidachitika ndi chani ?.....

Tsatirani tsamba ili la uthenga wabwino Masiku akubwerawa .



MASOMPHENYA, MALOTO NDI ANENERI



WOLEMBA

DRAKE CHIMPENI

*Lidzafika tsoka
lotsatana-tsatana, kudzakhalan-
so mbiri yotsatana-tsatana,
ndipo adzafunafuna
masomphenya a m'neneri....
Ndipo popanda vumbulutso an-
thu amasauka...Ezikieli
7:26.,Miyambo 29:18*

Ndime ziri m'mwamba-zi, m'neneri Ezikieli poonetsa zochitika za masiku otsiriza ano komanso olemba miyambo akutionetsa kufunika kwakukulu kwa **masomphenya**. Ezikieli wati anthu adzakhala akufunafuna masomphenya, kufunika kotere ndikwakukulu. Kufunika kotere kwa masomphenya sikungavetsetseke ngati sitingayankhe ena mwa mafunso adzaza maganizo a anthu ambiri, omwe Khristu akwaitana kumene kukhola lake.

kodi masomphenya ndi chani?

Nanga kufunika kotereku kukudza chifu-kwa chani?

Kodi amachokera kuti nanga kwa ndani?

Inutu muli ndimafunso abwino ndi ofunika pokhala nacho chidziwitso ,ndipo Mulungu atiyankhatu onse m'magazine uno.

Tiyeni poyamba kuvetsa tibwere kaye kuchiyambi munthu asadachimwe kudziko kulibe uchimo.

MULUNGU *adalenga anthu oongoka mntima* (Mlaliki 7:29), Ndipo lidali khumbo la Mulungu kuti munthu olengedwa muchifanizo chakeyu akhale ndikhalidwe la Umulungu . Potero makolo athu oyambirawo adali kulandira malangizo ndi chitsogozo kwa Mulungu polumikizana maso ndi maso opanda munthu wina ngati mkhala pakati.

Koma atachimwa Adamu ndi Hava sakadathaso kulumikizana ndi Mulungu monga poyamba paja. Chifukwa palibe amene angaone Mulungu ali ochimwa ndikukhala ndi moyo. Kotero Mulungu posafuna kumusiya munthu ochimwayu opanda chiyembekezo ndi chitsogozo , Iye adapeza njira ina yolumikizirana ndi munthu .Monga anena

'Pakakhala m'neneri pakati panu , INE Yehova ndidzindikiritsa kwa iye m'masomphenya, ndinena naye mnkulota.

(Numeri 12:6).

Kufika tsopano ndikhulupirira kuti tiri limodzi .komabe ena angati' ifetu brother tisadavetsebe kuti masomphenya ndi chani'.

Masomphenya ndinjira yomwe Mulungu amagwilitsa ntchito polumikizana ndi anthu ake koma osati mwachindunji(indirect).

Mwa njira ina kulumikizana uku kumachitika pakati pa Mulungu ndi anthu ake kugwiritsa nthito mkhala pakati otchedwa **m'neneri** wa Mulungu.

Ndicholinga cha Mulungu ndithu kuti anthu ake aziuzidwa ndi kulandira chitsimikizo , kudziwa komanso kuvetsetsa osati nthawi zomwe akukhala zokha koma zomwe ziri mnkudza.

Pakuti Ambuye Yehova sadzachita kanthu osaulula chisisi chake kwa atumiki ake aneneri

(amosi 3:7).

Ngati lero atumiki a UTHENGA wabwino angaime ndikuchita umboni zakubwera kwa Yesu posachedwapa , ndikufunika kwa kulapa pamene nthawi yayandika, iwotu amakhala otsimikizika mntima chotere chifukwa masomphenya olembedwa zaka masauzande zapitazo adaneneratu za nthawi tikukhalamoyi.

Mukhoza kuona kuti masomphenya ofotokoza za m'tsogolo ali ofunika kwambiri potiuza choyenera kuchita pamene nyengo yake yakwaniridwa.**werengani Mika 3:6**

Khristu amachita nawo motani mntima okaika ngati masomphenya angakwaniridwe?.

Masomphenya amatha kunena zomwe zidzachitikwe zaka zambiri zomwe zikubwerazo. Kotero owerenga ngati samvetsa amatha kukhumudwa popita nthawi zitasiyana ndi chiyembekezo chake ndipo amati 'masomphenya alephera'.

Koma khristu anena m'mau ake. |

Tiri nawo mau achinenero amene muchita bwino kuwasamalira monga nyali younikira mudima...pakuti masomphenya alindira nyengo yoikidwiratu ndipo afulumira potsiriza pake, osanama ,akachedwa uwalindirire popeza afika ndithu osazengereza.

2 Petro 1:19, Habakuku 2:3

To be Continued.....

Mzimu wachinenero

Thupi limafuna zina, Mzimu nawo umafuna zina iyi ndi nkondo. Ambuye Yesu sadatsiye ozingwatu koma adatilonjeza kuti tidzalandira Mzimu Woyera ndipo Mzimuyo adzatipatsa ife mphamvu zochita za mphamvu mu DZINA la AMBUYE wathu YESU.

Mphatso imodzi yomwetu MZIMU WOYERA amapereka ku mpingo wa Mulungu, mmene iye akufunira ndi Mzimu wachinenero. Mphatso iyi akuti tiyifunistsitse. 'Tsatani chikondi; koma funitsitsani mphatso zauzimu, koma koposa kuti mukanenere.'

1 AKORINTO 14:1

Nthawi zambiri mu mbiri a ayuda amalimbana ndi adani a Mulungu mu nkondo. Munthu wodzodzedwa, mtundu wosankhika inu makumana ndi nkondo. Akafunsira kwa YEHOVA, nakonza khalidwe lawo, Mulungu amawayankhula za mmene nkondo ikayendere!

Mzimu Wachinenero amayankhura choonadi. Mpikisano uliwonse umakhala ndi zovala zake zoyenera kuti munthu apambane. Mpikisano ukakhala oyika moyo wamunthu pachiponso, zovalanso zodzitetzera zimakhala zolimba kuti ngati munthu angagwe kaya mdani kumukankha moyo utetezeke.



Msilikali wavala zodzitetzera akupemphelera chitetezo chake ndi anthu ake.

MZIMU WA CHINENERO NDI CHANI?

Mzimu wa Chinenero umanena za YESU Khristu ndipotu zonena zake zimagwirizana ndi MALEMBA OPATURIKA a M'bible. Yohane mlembi wa buku la chibvumbulutso adaona masomphenya zinthu zomwe ziyenera kuchitika

M'masomphenyawa m'ngelo otumikira adanthauzira MZIMU wa CHINENERO motere pa Chibvumbulutso 19:10

Ndipo ndinagwa pa mapazi ake kumlambira iye, Ndipo ananena ndi ine, Tapenya, usatero; ine ndine kapolo mnzako, ndi mnzao wa abale ako akukhala nao umboni wa Yesu; lambira Mulungu: pakuti UMBONI WA YESU NDIWO MZIMU WA CHINENERO.

Satana ali nawo udani waukuru ndi osunga malamulo khumi a Mulungu ndi kukhala nawo umboni wa YESU—Chibvumbulutso 12:17. Mzimuyu amachitira umboni za Ambuye YESU Khristu pakudzudzula, kuchenjeza, kupereka chitsogozo m'njira zathu kudzera mwa aneneri ake. Anthu a Mulungu akadzichepetsa, napempha chitsogozo, Mzimu wa chinenero amafikira mmodzi mwa a khristuwo kudzera mmaloto ndi mmasomphenya. Mzimuyi wakhala akuyankhula ndi anthu chiyambireni chilengedwere cha dziko ndipo, nthawi zambiri amamunon'goneza ofunistsitsa nkhope ya Mulungu kuti tsegula bible, kaya zolemba izi werenga pakuti-pakuti, Munthu akawerenga amazindikira choonadi chonse, naphunzira mmwemo.

MPHATSO IMAPEREKEDWA KWA AMENE MZIMU WA MUSANKHA.

Mzimu wachinenero ndi wokhazikika mpakana kubweranso Ambuye YESU. Mau achinenero ndi monga nyali younikira m'malo a mdima. Mzimu wa chinenero ndi mphatso yomwe MZIMU WOYERA amapereka kwa Munthu yemwe wasankhidwa. “ndi kudziwa ichi poyamba, kuti palibe chinenero cha lembo chitanthauzidwa pa chokha, 'pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula. 2 PETRO 1:19-21”.

Mzimu wachinenero, unalipo mchipingano chakale, nthawi ya atumwi adawaunikira mmaulendo awo onse pokhazikitsa chi Khristu ndipo udzakhalapo kufikira kubwera kwa Yesu Khristu pozindikira kuti Ufumu wa Ambuye wayandikira.

NDAKATULO



Mphatso kulakatula ku Mzimba,

MUNDIKHULULUKIRE

Atate Anga Muli M'mwamba, Wachikhulupirilio ndiponya maso anga kudenga, ndidziwa uko m'komwe INU-Muli. Ndi mtima osweka ndadza pamaso panu uku nkuyankhula mosisima, msozi ukuyendera misese ya m'masayamu. Ndikumveratu chisoni kamoyoka, maphunziro atandinyenga zoti kulibe INU, Scince ikukanitsitsa kwantuyagalu. Ndinayala mkeka kudzikoku, nditakhala mwamtambasale, zaliwu lanu mku-mamva koma nkangoumisa mtima monga tanthwe. Muichi sindine oyenera kutchedwa mwana wanu.

Ndidapanduka nkukhala m'dani wanu pakuchita zomwe inu simukondwera nazo. M'mzikhatho zanga mwazala ndi mwazi wa anthu osalakwa. Ndaveka umasiye khwimbi la ana andi amayi pakuchosa miyoyo yazibale awo. Ndi cholinga chokondweretsa ine mwini. Nkumakasanganalala ndi akazi m'makukamu, pomwe ena akulira Kamba kazochita zanga. Ine mkumati umenewo ndi moyo. Osadziwa ondyinyenga nkukhala Lucifer chinjoka choipacho.

Monga mwa mau anu nthawi ndi nyengo munayitaira pachabe, Ndidziwa musakasaka yotayikayo. Imodzi mwayiwo ndine ndili pano. Lembani dzina langa m'buku la woyera mtimawo. Sambiseni nkhalé monga mufunira. Pakukhala ine ndakuchimwirani inu. Ndi mtima osweka ndadza nawo moyowu, mmene ndiliri. Ndidziwa mundirandira mokondwa waumbandane, wakuba ndili pano,

Mkhulukireni Atate.

Masalmo 51:1-19

30/05/2025

TILI PATI MU ULOSI



Ndipo ngati ndipita kukakonjera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso.

Ulosi uwu kuyambira pa tsiku lomwe Yesu adalankhula patangodutsa nthawi pang'ono atabatizidwa mu AD 27 kufikira tsiku lomwe Yesu Khristu abwere, dziwani kuti pa nzere umenewu Pali zochitika zambiri zomwe zichitike moyang'anizana ndi Kudza kwake.

Mchaka cha 31 AD pamene Yesu adakhala pa phiri la Azitona ndi ophunzira Ake, kucheza nawo, Iye adawafotokozera mmene moyo ukhalire kufikira Kudza kwake Mateyu 24:3

Ndipo pamene Iye analikukhala pansi pa phiri la Azitona, ophunzira anadza kwa Iye pa yekha, nanena, Mutiuze ife zija zidzaoneka liti? ndipo cizindikiro ca kufika kwanu nciani, ndi ca mathedwe a nthawi ya pansi pano? Funso ili likuonetsera chidwi chomwe ophunzira akalelo adali nacho pa Kutha Kwa nthawi ya moyo Uno komanso



ndasankhidwa tsiku ndi tsiku ndimaona kuchedwa, ndipo chiyembekezo changa chidali chodaladi. Usiku wina ndikugona ndidalota ndili pa kapinga obiliwira bwino, Malo ozunguliridwa ndi mitengo yabwino, kamphopo kakuomba bwino,,

Dziwani kuti Yesu abwere ndithu ndipo inu ndi ine tiyenera kukonzekera podzuka mmawa ndidadzuka okondwa koma sindidamvetsetse tanthauzo la lotoli.... Koma tsiku lomwe mchemwali Wanga oyamba kubadwa kwathu "Leah" adanditenga kukandisiya Ku sukuluyi mpamene tidali kulowa pa chipata cha sukuluyi mpamene loto langa lonse lida yamba kutambasulidwa bwino.

Maso anga adaona mitengo yokongola ikuluikulu,,ndidamva nkokomo wa madzi a mtsinje wa Mulunguzi,,maso anga adaona kapinga obiliwira bwino kwambiri,,sukulu idali yokongola kwambiri,,sindikudziwa pano. Moyo Wanga udadzadzidwa ndi chimwemwe komanso chiyembekezo chokwaniritsidwa chidaku ubongo Wanga

Taganizani za tsiku lomwe Yesu abwere Pakutha pa Ulosi wakudza kwake,titadutsa mavuto a dziko ili lonse,,kuletsedwa kugula ndi kugulitsa, kukakamizidwa kupembedza dzuwa,,maudani,Kupasuka Kwa m'banja,nkhondo,miliri ndi zina zambiri...moyo wathu udzakondwera Poo-na dziko Lokometsetsa Yerusalemu Watsopano.

Kudziwa komwe tikuchokera, pomwe tili ndi komwe kwatsala kuti Yesu abwere kudzatitenga

Tito 2:13

akulindira chiyembekezo chodalala, ndi maonekedwe a ulemmerero wa Mulungu wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Kristu;

Ichi ndi chiyembekezo chimene munthu wina aliyense okhala pano pa dziko lapansi ayenera kukhala nacho chifukwa Kuli moyo wina wabwino ukatha moyo Uno.

TILI PATI MU ULOSI?

Munthu ungakumane ndi mavuto oliza chotani koma chiyembekezo ichi tiyenera kukhala nacho Chiyembekezo chodalala ichi chidzakwaniritsidwa pamene Yesu abwere ndi khamu la angelo

Dziwani kuti liu la ulosi, kapena kuti kunena zodzachitika kutsogolo Kwa nthawi ya moyo Uno zidalembedwa; zokhudza mafumu a dziko mmene ayendere,

chizindikiro cha kudza Kwa Yesu Khristu kwachiwiri.

Poyankha Yesu adawaonetsera za Zizindikiro,zomwe zilingati zikwangwani zoonetsera kutalika kapena kufupikira Kwa ulendo wakubwera Kwa YESU kudzatitenga.. amenepa ndi pomwe tikufunsa kuti "Tilipati Mu Ulosi" Ulosi wakudza Kwa Yesu Khristu kwachiwiri

Ndimakumbukira nthawi imene ndinakhonza mayeso a standard 8 kupita kukayamba maphunziro a Secondary Ku sukuru yotchedwa Mulunguzi m'boma la Zomba, mmoyo Mwanga mudali chimwemwe choposa ndipo kuyambira tsiku limene ndidauzidwa kuti

WOLEMBA:

EV. YANKHO MALIZANI



<< Kuchokera ku tsamba 7

Mzimu wachinenero

Chotero Mzimu Wachinenero ndi mlozo wabwino otitsogolera anthufe kukhala ndi chiyembekezo chodala chakudza Kwa Yesu Khristu. Chifukwa choti nthawi ya kumapeto ino nkondo ikula kwambiri kuposa Pachiyambi Mulungu watipatsa chida champhamvu ndiye Mzimu Wachinenero. Mutsatire bwino maphunziro awa ndipo muzindikira bwino komwe mukulowera ndi moyo wanu. Mudziweni Yesu lero. Ambuye akudalitseni chifukwa chowerenga tsambali.

ZAKUDYA ZA THANZI LABWINO

By Food Evangelist Mrs B Kabanga



CHOCHO PIZZA

Idyani payokha. Komanso nthochi yophika/mpunga ndi tomato 🍅 sauce

SERVINGS: 8 PREPPING TIME: 20 MIN COOKING TIME: 30 MIN

INGREDIENTS

- 3 Chocho Squash
- 2 Carrot 🥕
- 1 cup Zitheba 🌿
- 1 Garlic bulb 🧄
- 2 Anyezi 🍎
- 1/4 cup Nsawawa 🌿
- 1 Green pepper 🌶️
- 1 Red pepper 🍅
- 1 cup bread Flour
- Salt to taste
- 1 tsp Turmeric
- 3 Tbsp Cooking oil

DIRECTIONS

1. Tsukani masamba onse. Chocho(Chayote) ndi Carrot musende makoko ake.
2. Dulani ma piece ang'onoang'ono a zonse.
3. Mu basin lokulilapo, phatikizani masamba onse yomwe mungakonde
4. Wazani mchere wa table salt, turmeric ndi spice yomwe mungakonde
5. Thirani 1 Tbsp mafuta ophikira
6. Thirani flour mpaka zioneke ngati mwaika cream
7. Kwa amene muli dzira la nkhuu zalokolo, mukhoza kuyikamo.
8. pakani mafuta mu tin/ mpoto/ pan yomwe mu bakery
9. Ikani mobakera 350° c / kapena mu flying pan yaikulu (makala ochepa PANSI ambiri pamwamba.)
10. Yamikani Mulungu popereka Mphatso yakupatsa kudya.. Sangalani ndi apabanja anu.

NOTES

Mmalo mwa Chocho(Shushu/ Sayote), mukhoza kuikapo, mbatatesi, kaya MBATATA or chinangwa. Komanso mmalo mobakera mungathe kukazinga. Shushu payekha ndi ndiwo.!

TILI PATI MU ULOSI

Cibvumbulutso 21:1-4 Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano; pakuti m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka, ndipo kulibenso nyanja.

Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wace.

Ndipo ndinamva mau akuru ocokera ku mpando wacifumu, ndi kunena Taonani, cihema ca Mulungu ciri mwa anthu; ndipo adzakhalisa nao, ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao; ndipo adzawapukutira misozi yonse kuicotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhhalanso imfa; ndipo sipadzakhhalanso maliro, kapena kulira, kapena cowawitsa; zoyambazo zapita.

Musalole kuti zovuta za moyo uno zikulepheretseni kudzapezeka mu dziko lokomalo. Tiyeni tikhalire limodzi mu gawo Lina, phunziro ili pamene tidzikhalala, tikukambirana mwezi ndi mwezi...

Ambuye wathu YESU KHRISTU, amakukondani

Nawa mafunso Ku moyo wanu

1. KODI YESU MUDAMULANDIRA KALE KUKHALA AMBUYE NDI MPULUMUTSI WA MOYO WANU?

Dziwani mukhonza kuvomereza ndi kulapa ntchimo lanu lero nthawi yomwe ino pamene mulipo ndipo Yesu adzakulandirani

2. KODI MUNAPANGA KALE CHISANKHO CHOBATIZIDWA UBATIZO WA MMADZI OSATI PA MPHUMI? chifukwa

iyi ndi Njira ya YESU Mbuye wathu, pangani chisankho lero nthawi idakalipo

""Yesu akufuna akhale bwenzi lanu kuti adzakutengeneni akamabwera"

Zikomo kwambiri chifukwa chowerenga gawo loyambali.

WOLEMBA:

YANKHO MALIZANI.



WOLEMBA
EV. YANKHO
MALIZANI

SABATA KAPENA SUNDAY

30/05/2025

Dziko lapansi liri pa nkondo yaikulu imene imatchulidwa kuti Mkangano waukuru. Ndipo aliyense okhala pa dziko lapansi ali ndi mbali yomwe akutenga mochita kusankha kapena ayi.

Nkhondo iyi idayamba ndipo ikhala ndi mathero ake. Koma funso nkumati Kodi nkondo iyi ikamatha iwe ngati munthu usankha mbali iti? Yomwe ili yopambana kapena yogonjetsedwa.

Buku lopatulika Bible nkhekwe ya mabuku a alembi osiyanasiyana lidafotokoza za chiyambi cha nkondo iyi.

Cibvumbulutso 12:7-9

Ndipo munali nkondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ace akucita nkondo ndi cinjoka;


cinjokanso ndi angelo ace cinacita nkondo; ndipo sicinalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m'mwamba.

Ndipo cinaponyedwa pansi cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi. ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi.

Mmalemba awa mmene akuti **Mikayeli** akutanthauza kuti **YESU** chifukwa dzina loti Michael (Mikayeri) limatanthauza kuti **Iye amene ali monga Mulungu**

Ndipo chinjoka ndi satana

Satana ataukila kumwamba adathiridwa nkondo ndipo adaponyedwa kuno Ku dziko pamodzi ndi Angelo Ake omwe lero timawadziwa kuti ndi ziwanda.



Tiyeni tidziwe ichi mbali ziwiri za nkondoyi zidayambira pamenepa, ndipo satana uyu ndi Angelo Ake akugwa ali pakati pa ife anthu ngakhale matchalitchi, mizikiti ndi Malo opembedzera ambiri amapezeka, tsoka ilo ngakhale mmabanja ambiri ndipo mitundu ndi zikhalidwe zambiri zimatsogozedwa ndi Angelo akugwawa.

Chofunika kudziwa kwambiri ndi choti khalidwe lake loukira, kutsitsa pa choonadi cha Mulungu iye sadalisiye chifukwa ndipo pagona nkondo yake.

Kodi inu panokha muli mbali yotsutsa choonadi cha Mulungu kapena muli mbali ya Mlengi wanu?

Mu Mbiri ya dziko lapansi anthu akhala akupanga zisankho kukhala mbali ya Mulungu kapena satana.

Pa **Eksodo 32:25-26** Tikupezapo nkhani ya Israel atayika kusiya Mulungu Mlengi, nkuyamba kulambira satana, anthu adamuzunguza Aroni, mpakana iye adagonjera Ku chifuniro chawo. koma Mose pobwera zidamukhudza ndipo adawafunsa anthu kuti apange chisankho kukhala mbali ya Mulungu kapena ayi.

.Ndipo pamene Mose anaona kuti anthu anamasuka, popeza Aroni adawamasula kuti awatonze adani ao,


Mose anaima pa cipata ca cigono, nati, Onse akubvomereza Yehova, adze kwa ine. Pamenepo ana amuna onse a Levi anasonkhana kwa iye,

Leronso anthu tiyenera kuchita chisankho kulambira Mulungu Mlengi kapena satana mdaniyo.

Cholembedwa ichi chitsindika kwam-biri pankhani ya Sabata La Yehova tsiku la nambala **7(Saturday)** kapena tsiku loyamba lapa mulungu **(Sunday)**. Izi zilichonchi chifukwa awa nde masiku akuluakulu mchিপembedzo omwe magulu otchedwa opembedza Mulungu Mlengi at-samirako.



SABATA KAPENA SUNDAY



Koma podziwa kuti tapeza moyowu uli ndi mbali ziwiri zokha basi; Mulungu Mlengi kapena satana mdierekezi, kuwala ndi Mdima, kumanja ndi kumanzere munthu ayenera kusankha mbali imodzi ndipo mkwabwino kwambiri kusankha mbali yoyenera yomwe Kuli Mulungu wotilenga ndi wotipatsa moyo.

Opembedza omwe amagwiritsa ntchito tsiku la **SABATA** amafotokoza zifukwa zawo zotsamira Ku chisankho chawo, komanso nawo omwe adasankha Sunday, alinazo zifukwa zomwe amapembedzera Mlengi wao patsikuli. Koma tidziwe kuti mbali zonsezi sidzingakhale zolondola cholondola chiyenera kukhala Sunday kapena Sabata.

MU cholemba ichi tisanthula malemba okhudza Masiku awiriwa komanso kuona Mbiri ya dziko lapansi zomwe idalembe m'ma buku ake.

Yesu Khristu Mbuyeyo akuphunzitsa pokamba za mbali ziwirizi adati

Mateyu 7:13-14

Lowani pa cipata copapatiza; cifukwa cipata ciri cacikuru, ndi njira yakumuka nayo kukuonongeka iri yotakata; ndipo ali ambiri amene alowa pa ico.

Pakuti cipata ciri copapatiza, ndi icepetsa njirayo yakumuka nayo kumoyo, ndimo akucipeza cimeneco ali owerengeka.

Inu musankhe mbali.

Mwina mmene mwangowerenga pang'ono cholembedwachi mtima wanu wakhudzika kale ndipo mukufuna kuchita chisankho.

Musachedwe poti za mmawa sizidziwika. Lero ndilo tsiku labwino. Mukhonza kugwada mnyumba mwanu, kapena pomwe mwakhalapo powerenga tsambali mukhonzanso kulankhula ndi Ambuye kupempha kuti Yesu Mpulumutsi Wanga thandizeni kusankha mbali yolondola ndipo mupange chisankho chowerenga Bible panokha, osati mwaganizo la mpingo, ayi, koma inuyo monga munthu opangidwa mchifanizo cha Mulungu Atate wanu.

Mukhonzanso kuyimba foni Ku nambala zomwe zili kumapeto Kwa Magazine ino. Ndikufunirani zabwino zonse mchisankho chanu. tidzakumanenso mwezi wammawa.



**WOLEMBA
YANKHO MALIZANI**

ANABADWIRA KUTI?

Ngati munthu Aliyense M’busa Keros Francis Grem anabadwa m’banja la ana asanu ndi awiri ndipo iwo anabadwa ngati mapasa ndi M’chimwene wawo. M’busa Keros Grem anabadwa m’chaka cha 1982 pa 23 March. Iwo anabadwira ku Blantyre pa chipatala chija cha Queen Elizabeth komwe makolo awo amkagwira ntchito. poti bambo awo anali ochokera ku Thyolo ndipo mayi awo anali ochokera ku Ntcheu, mudzi wa Doviko. Komwense ndi ndi kumudzinsoko kwa M’busa Keros Grem.

MAPHUNZIRO

Ngati mwana anayamba ma phunziro awo a chala cha mkamba mphala pa Sukulu ya Nyambadwe Primary, komwe anayamba kalasi yoyamba mpaka ya chinayi, kamba ka kudwala kwa mayi awo.

mu chaka cha 1995 anachoka kupita ku mudzi kwa mayi awo kwa Doviko ku ntcheu, komwe anakapitiliza ndi kulemba mayeso opitilila ku sekondale. Anachita mwayi kusakhidwa ku St Kizito Seminary ndipo mu m’chakachi

anasakhidwa anyamata awiri okha. Koma kumeneko maphunziro sanapitilire kamba ka mavuto a zachuma. ngakhale ili silinali khumbo lawo kuchoka poti anali kufunitsitsa kudzakhalwa wa msembe.

*Akusekelera anati,
“ndamangapo ma sikero ine
kuti tikhale ndi katundu
wambiri mwachinyengo.*



Mu m’chaka cha 2001, anatsatira bambo awo ku Nchalo komwe anakapitiliza maphunziro pa Nchalo GDSS mpaka kalasi yomaliza ya ku sekondale. Kamba ka mavuto a mavuto

Mavuto azachuma omwewa maloto opitiliza maphunziro anafufutika kotero analowa mtauni ya Blantyre mkuyamba kugwira tchito kwa anzathu achimwenye ataona kuti sizikuyenda anabwellerera ku nchalo komwe anayamba kugula nthonje. Pofufuza mbiri ya mkuluyi ananena motsindika kuti mu ntchito yogula nthonje munali za chinyengo

Moyo wa banja wa M’busa Keros Grem

Ali mkati mogwira ntchito yogula nthonje, ndalama zinayamba kupezeka ndipo maloto ofuna kukhala wamsembe anachepa kotero anapeza banja.

Kwa mkazi yemwe mu mumkucheza kwathu anamulongosola monga “Mkazi odziwa mavuto, opilira komanso n’thandizi mu utumiki” kwinaku akumwemwetera kutsimikizira izi. Abusa a Keros Grem analowa m’banja ndi Ellah Machonga mu chaka cha 2007 ndipo awiri Mulungu wa adalitsa ndi ana Atatu akazi okhaokha.

Nditawafunsa za chimwemwe chawo pa ana akazi okha okha analakhula mokonda kuti “Mulungu salakwitsa popeza kwao anabadwa anyamata asanu ndi Modzi ndi mkazi modzi. ndipo anawa ndi mphatso yopambana kwa ine

ULENDO WA MOYO WA UZIMU

Ndinabatizidwa mu mpingo wa katolika ndipo ndipo nditabatizidwa khumbo tsopano lotumikira monga wa msembe linabadwanso kotero nditabatizidwa ndakhala ndikutumikira mokhulupilika ngati mu kwaya ija yotchuka ya St Cecilia, ndakhalaponso nkhalapampando wa limana, ndi kutumikira ku council. Ngati mkatolika ndinali ndi ganizo limene timaphunzitsana kuti kuguwa kuja Yesu Kristu amafikako ndiye ndinali okhulupilika kwambiri kumpingo. Mu 2020 kunatuluka mwayi wofuna azibusa a pa mpingo ndinalembera mpaka ndinachita mwayi mu nthawiyo ndinakhoza bwino kwabasi.

IKUPITILIRA.....



Chodabwitsa kwambiri ndika malalika anthu anakhala akuyamikira, koma ine mwini sindimkadziwa kuti ndi mphatso yotani imene ndinali nayo. Kumene kunjani ndinali ndimwayi olova m'zipinda za amsembe komwe ndi mapeza ma pemphera pakhoma amene amsembe amapemphera asanayambe .mwambo wa misa.

Mu chaka cha 2021 ndinapatsidwa mwayi wolalikiranso Ndipo ndinali kulalikirira buku la Machitidwe 3, Pomwe ndimadzudzula anthu za kukhala mu mpingo koma mkumakhalanso ndi zibwezi, akazi a eni ake komanso ana a kwaya.

“Koma inu ndinu Badwa yosakhika, ansembe acifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wace, kotero kuti mulalikire zoposazo za iye amene anakuitanani muturuke mumdima, mulowe kuunika kwace kodabwitsa.”

Sindinadziwe kuti kulalikirira uku akuluakulu ena sanakondwe nako kuphatikiza bambo mfumu a a parish imeneyi. Ndipo kuti ndiziwe kuti ndapalamula ndimavera mauthenga ena kuchokera kwa bambo mfumu akamalalikirira, Mu maulaliki awo amalakhula kuti ena a inu mumadzimva ngati mumalalikirira koma mphatso mulibe, mumalakhula zonyozetsa mpingo.

Ataona kuti ma uthenga awa sakundisutha anayamba kundiimbira phone usiku kuti zomwe ndi ngazionezo iwo ziwakhudze. Ndinali ndi mantha koma sindinasuthike chifu kwa ndinalibe ganizo kuti mu mpingo anthu amatha kuchitana zoipa.

“Galimoto ya mpingo inakanditsitsira pansi pa mtengo”

Dzidzidzi tsiku lina ndinangomva kuti basi inuyo abusa mwasamutsidwa, Panalibe zokambirana ndinakasiidwa kumudzi kwathu komwe mu mthawiyi nyumba yanga inali itagwa ndi namondwe wa ana. Ndipo kunena monenetsa galimoto ya mpingo inakanditsiya pansi pa mtengo. Ndipo pondisiya anandilonjeza kuti tibweranso tidzalongosole za nyumba...

Koma kuchokera pamene po sanabweranso mkomwe.

Unali moyo wovuta, kuchokera mtauni kukaponyedwa pa mudzi popanda nyumba. Abale anga ndi amene anandipatsa pobisala.

M' busa Grem Monga Mlaliki wa Uthenga wa-kumapeto

Ndinapanga chisankho choyamba kupemphera mpingo wina, patatha nthawi ndipo nditaunguza bwino lomwe ndi banja langa tinalimbikitsika mtima kuyamba mpingo wa Seventh Day Adventist. chifukwa cha chidwi ndi kulalikirira uthenga abusa athu a m'chigawo anandilumikizansitsa ndi kagulu kena kolalikirira uthenga wa kumapeto wa Angelo atatu . Ndipamene ndikupeza mu gulu limeneli kufikana tsopano lino.

Mau amene amakhala pa mtima panga ndi I petro 2:9,25.

“Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za iye amene anakuitanani , mutuluke mumdima, mulowe kuunika kwake kodabwitsa”

“Pakuti munalikusochera ngati nkhosha; koma tsopano mwabwera kwa Mbusa ndi Woyang'anira wa moyo wanu.”

Nditadziwa choonadi cha sabata ndinapanga Chisankho Chopilitiza kulalikirira uthenga umene ndi makhulupilira kuti Mulungu anaikizira pa moyo wanga kuyambira pa chiyambi..... Ndiko kutchula ntchimo ndi dzina lake.

LANGIZO LANGA KU DZIKO

Yesu akubwera posachedwapa ndipo tikuyenera kulandira yesu Khristu akhale Mbuye ndi Mpulumutsi wa miyoyo yathu.



WOLEMBA:
END TIME MESSENGER
LUKE CHAPULI



INU NDI THANZI LANU

Ndilandireni mwa chimwemwe ndi mwamsangala ku tsamba lathu loyamba kusindikizidwa mwezi uno wa May, chaka chino cha 2025.

Mutsambali tikhala tikumakambirana za inu ndi thanzi lanu mudzikhala ndi ine Mdingo Marsen Nyambi

MALANGIZO A ULELE A MULUNGU PA NKHANI ZA THANZI

Munthu yemwe umamukonda ndi amene sumaumira kumupatsa malangizo chifukwa Mulungu ndiye chikondi *Iye wasakonda sazindikira Mulungu ; chifukwa Mulungu ndiye chikondi* (1 Yohane 4 v 8)

Kodi inu mukudziwa kuti ndizotheka kukhala ndi moyo opanda Madotolo ndi Zipatala ?

Kungotero kokhako kutereko mwadzifunsa kale, kuti koma awa akulemba pa tsambali akuganiza bwanji ? Ayi ndithu ndi zowona zenizeni.

Chowonadi ndi chakuti anthu ochepa okha ndi amene amapita kuchipatala pa nthawi, taganizani za chiwerengero cha anthu a mdera lanu, ndiye mudzifunse kuti ndi angati omwe amakhala kuti akudwala. Njira yokhayo yosadziwira dzina, mavalidwe a madotolo ndi kudzisamalira wekha, kudzisamalira motani ? Akatswiri ofufuza a sayansi, akhala akuchenjeza za mafuta ena otchedwa (cholesterol), fodya, kutopa, kunenepa kwambiri mowa ndi zina. Ndiye bwanji osalingalira izi,

Zipatala zambiri za padziko lapansi zikudzaza ndi anthu omwe ananyozera malangizo athanzi. Kodi inunso mukufuna mutakhala gulu logona mchিপatala ? Kutereku mwakana mumtima mwanumo, koma nanga zijazi.

Anthu ena amaganiza kuti Mulungu salabadira nkhanu za thanzi, eti munthu angakaonongedwe chifukwa cha nkhanu ya thanzi, aaah nkhanu yosautsa.

Kodi simudziwa kuti muli Kachisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu ? Ngati wina awononga kachisi wa Mulungu, ameneyo Mulungu adzamuononga ; pakuti kachisi wa Mulungu ndi wopatulika, ameneyo ndi inu. (1Akolinto 3 v 16, 17)


Mutsambali tikhala tikukambirana zambiri zokhudza thanzi lathu, muchita bwino inu kumatsatira ndi chidwi, chifukwa tidzigawana zinthu zina zomwe simunamvepo chibadwireni, komanso kukumbutsana zomwe tinamva kale.

Mulungu anapereka malamulo a zathanzi pofuna kuti tikhale ndi moyo wathanzi komanso wokondwa. Ndipo Yehova anatilamula tizichita malemba awa onse, kuti atisunge amoyo, monga lero lino. (Deutronomo 6 v 24)




Kuitanira kwa uthenga wabwino sikuyenera kupita kwa anthu osankhidwa ochepa okha, amene ife tikuganiza kuti akaumva awugwilitisa ntchito. Uthenga ukuyenera kupita kwa aliyense, chifukwa aliyense akufuna moyo, Mulungu akamadalisita amatidalitsa kuti ifenso tikafikire anthu ena.

Mulungu anapereka malamulo a za thanzi chifukwa akudziwa choyenera mmatupi mwathu, chimodzi modzi okonza njinga zamoto kapena galimoto iwo amapereka kabukhu kofotokoza kagwitsidwe ntchito kanjinga kapena Galimotoyo chifukwa iwo amadziwa mmene katundu wawo angagwilire ntchito bwino. Nthawi zonse matenda samangobwera opanda choyambitsa. Umachita kuwaitanitsa, ngati mmene timalemba kalata yofuna kanthu kena kwa wina. Zingathe kumveka mwachilendo kuti kodi mlembiyu koma amatha kuyankhula bwino, ndithu zowona zeni zeni. Tikangonyozera malamulo omwe Mulungu anapereka, pamenepo kalata yathu imakhala yayankhidwa basi. Chimodzomodzi ana amene samvera malangizo abwino a makolo amakumana nazo.



**WOLEMBA
MARSEN NYAMBI**



WOLEMBA

MARSENNYAMBI

INU NDI THANZI LANU

Anthu ochuluka zedi akuwonon-geka chifukwa cholephera kutsata malamulo a thanzi monga madyedwe, mamwedwe, mavalidwe ndi kagwiridwe kantchito. Inu zikukuthekerani bwanji kapena anzathu muli bwino ? Anthu ambiri akayamba kudwala amayiwala kuti anaswa malamulo a za thanzi omwe Mulungu anapereka ndiye amayamba kudandaula kwa Mulungu pamene Mulungu sizikumukhudza olo pang'ono .



.Akulu akale anati “Mwana akalilira nyanga ya msatsi, msemere imfotere yekha. Ndiye ine kapena inu mukadwala sivuto la Mulungu ko-ma vuto lathu. Mulungu sanapange munthu kuti adzadwale. Mulungu anatipatsa mphamvu zapadera . Anatipatsa ziwalo zomwe chili-chonse chili ndi ntchito yake ndipo zimathandizana kagwiliodwe ka ntchito. Nthawi ina tidzagawana mmene ubongo wathu umagwilira ntchito tikamayimba ngakhale kuwerenga.

Uthenga wa nthawi yathu ino ukuyenera kupita limodzi ndi uthenga wa za thanzi, inu ndinu mboni ,mkhristu wodwalala kapena wofooka

Pamene tikuthamanga ndi uthenga wakuti titem-benuke mtima chifukwa



kubwera kwa Yesu Khristu kwayandikira kuposa momwe tinayamba kukhulupilira nthawi yomweyo tikuyeneranso kuwauza anthu kuti awope Mulungu ndi kumpatsa ulemerero wake. Komano ineyo ndingatenge bwanji uthenga omwe ineyo ukundivuta kumvetsetsa.

Paja chiweruzo chikuyamba pa nyumba ya Izrael ndiye ngati ayuda zawavuta ndiye zitha bwanji ndi anthu wamba.

Masiku ano otsiliza pakufunika amuna ndi akazi omwe sangagudwe kapena kugulitsidwa , omwe saopa kutchula tchimo ndi dzina lake , okhala ndi chikumbumtima chowona chimene chimayerekezedwa ndi ulusi ndi singano. Ulusi nthawi zonse umakadutsa pomwe singano yadutsa.

Komatu kuti izi zitheke simasewera , zikufunika kudzipereka kwa thunthu kwa Khristu Yesu.

Inuyo amene mukuwerenganu, maganizo anu ndi otani pa thanzi lanu ?

Kapena uthenga uwu ukubwera ngati chipozezo ?

Tiyeni tikumane mwezi wamawa , pa tsamba lomweli **LA INU NDI NTHANZI LANU.**

AMBUYE AKUDALITSENI

SITIDZIWA KUDZA KWA MBUYE



WOLEMBA SOLOMON LAPSON

◆ Khalani okonzeka nthawi zonse chifukwa tsiku lomwe simukulidzidwa Yesu abwera

◆ Sungani malamulo onse a Mulungu

◆ Gulani Bible mudziwelenga

ZINA ZAMU TSAMBALI:

- ◆ Mulungu ndi ndani
- ◆ Banja la Chikhristu
- ◆ Tili pati mu Ulosi
- ◆ Sabata kapena sunday
- ◆ Adziwani Atumiki anu
- ◆ Inu ndi thanzi lanu
- ◆ Maumboni a kutembenuka

Sitidziwa kudza kwa Mbuye ndi nyimbo number 181 yomwe imapezeka mu buku la mpingo wa Seventh day Adventist latchedwa Khristu mu nyimbo. Inapekedwa ndikulembedwa ndi Franklin Edson Belden. Belden anabadwira ku battle creek, Michigan, pa March 21, 1858. iye anali wa mpingo wa Seventh Day Adventist ndipo anali mwana wamkulu mwa ana asanu obadwa kwa Stephen Belden ndi Sarah Harmon Belden, mlongo wamkulu wa Ellen Harmon white. Anapeza maphunziro ake ambiri ku Battle Creek College. Belden anali okonda kuwelenga Buku lopatulika ndipo tsiku lina amkawelenga Mateyu 24 ndipo pa vesi 45-51 ndipomwe ana-pezapo nkhani yomwe inamupangitsa kulemba nyimbioyi.

"Mbuye wa akapolo adzafika tsiku losamuyembekeza iye, ndi nthawi yosadziwa iye."


Luso la Belden mu nyimbo zinasonyezedwa ndi chizolowezi chake cholembe nyimbo kuti zigwirizane ndi ulaliki pamene ukulalikidwa. Anatenga Malemba a vesili lapa Mateyu 24 kukhala mutu wake wa nyimboyi munga ulaliki.

CHOMWE MUYENERA KUDZI

Tsiku lakudza kwa Yesu layandikira kwambiri Kuti kusandulika kwa umunthu kuchitidwe, ndipo nthawi yotsalayo ndi yayifupi kwambiri.

Ambiri amanena kuti Yesu akuchedwa kubwera ndipo m'malingaliro mwawo akumati nditha kunjoya nalo m'dzikoli, namanena kuti adzalapa ndikuyamba kuchita kufuna kwa Mulungu kutsogolo pasalingalira za tsiku la imfa yawo. Nchifu kwa chiyani Yesu akuchedwa kubwera? Ndichifukwa chakuti Mulungu sakufuna kuti anthu ake awonongeke ndipo zaachititsa kuti achedwe kwa nthawi yaitali. Amene mukonzeka kubwera kwa Yesu Mulungu

akuti pitirizani kuchita zimenezo mpaka imfa yanu chifukwa kudzakhala kuuka kwapadera kwa iwo amene akudzikonzeke okha kubwera kwa Yesu. Kaya takonzeka kapena ayi, kaya tikhalebe ndi moyo kapena timwalira koma nkhani ndi yakuti Yesu akubwera posachedwa ndipo tili ndi nthawi yochepe yakonzekera



FRANKLIN EDSON BELDEN

Nyimbo yonse imati;

1. *Sitidziwa kudza kwa mbuye madzulo kapena mmawa; kapena nthawi ya usiku, kapena m'mabingakucha; atizatu tikonzeke tisazime nyali zathu, Pobwera adatipezetu tili kudikira iye*

CHORUS

Kudikiratu ndi kupemphera Kuchexeratu, Ndikuyang'anira inu

2. *Chikondi chake nchodwabwitsa, kuti-ombola ifetu; anasiya malo oposa, ndza kudzatiferatu; Nthawi zonse' amakondwera, Mmene owomboledwawo; Akondwera mchiyembekezo, podikira mbuye wawo.*
3. *Inu Yesu mombolo wanga, mudziwa ndikukondani; ndiyembekeza kundiona, ndidzamva mawu anuwo; Mmene mudzadza kuweluzana adzakuthawani koma ine ndidzakondwera, Ndili kudikira inu*

MAGAZINE YOTSATIRAYO



MBIRI YA ANTONIO SOLOMON BANDA.

Yemwe adali Rasta kwa zaka zochuluka , komanso oyimba nyimbo za reggae.....

Koma lero adasankha Yesu, ndipo ali mu mpingo wa Seventh Day Adventist.....

Zambiri zibwera mu mwezi wa June Ku-mapeto

ADZIWENI ATUMIKI ANU

1. Ndi oyani?
2. Anakula bwanji?
3. Anatembenuka bwanji?
4. Ali ndi unthenga wanji?

ZOZIZWA ZA MAKONO ANO

1. Chinachitika mchiani moyo wawo?

INU NDI NTHAZI LANU

Idyani, mlingo woyenera mu nthawi yake



BOOK NOW

Make your own Soap with me For Free



MAGAZINE YOTSATIRAYO

Tsatirani nkhani zikulu zikulu izi mu magazine ya June..... ➡

Breaking News 25

TEXAS AKHAZIKITSA LAMULO LOKAKAMIZA KUPEMPHERA SUNDAY



And what day is it
Texas Republicans just passed a bill forcing every teacher to post the Ten Commandments in their classroom



It's ironic
Talarico asked Noble which day the Jewish Sabbath falls on. She answered, "Saturday." He followed up by asking what day they were voting on the bill, which all knew was Sunday, the Christian Sabbath day. "It's ironic, isn't it?" Noble added with a smile.

[READ MORE](#) JUNE 2025
@ TILI PATI MU ULOS

ZILI NDITANTHAUZO LANJI KUTI PAPA LEO

WALALIKA KUTI IYE NDI MU ROMA?



23-25 DANIEL 7

[READ MORE](#)
June 2025
@ Tili Pati Mu ULOSI!

'I am Roman,' Pope Leo says, as he becomes the bishop of Rome

MAY 25, 2025 · 6:06 PM ET

 Clare Marie Schneider



Pope Leo XIV presides over a Mass in the St. John Lateran Basilica, formalizing his role as bishop of Rome in Rome on Sunday.
Gregorio Borgià/AP

- ◆ MUKAWERENGA APATSENI ENA AWERENGE.....
- ◆ MUKAPEZA MAGAZINE IYI PAMPANDO WERENGANI MUISIYE POMPA.....
- ◆ MAGAZINE IYI NDIYAULELE



W

otsatira aliyense wa

Yesu Khristu Ali ndintchito yoti agwire ngati mishonale Wa khristu m' banja , kwa oyandikana nawo, ntawuni kapena mu mzinda umene amakhala. Onse amene anapatlidwa ndi Mulungu amawapanga kukhala zida za chilungamo kuti alakhule kwa ena za kuunika kwa choonadi, chuma cha chisomo chake. Osakhulupilira angaoneke osalabadira ndi osasamala; komabe Mulungu akuchita chidwi ndikukhutilitsa mitima yawo kuti choonadi chili chenicheni.



End Time Messenger

Endtimesmessenger.repent@gmail.com

+265 995 249 973/88 42 08107